


Moyo wosatha kumwamba ndi mphatso koma tchimo limatilekanitsa ndi Mulungu. Kuchimwa ndiko kusankha kuchita zinthu zomwe tikudziwa kuti ndizolakwika ... kusilira, udani, umbombo, ndi zina zotero.

Baibulo likufotokoza kuti “*onse anachimwa ndipo anaperewera pa ulemelero wa Mulungu*” komanso “*mphotho ya uchimo ndi imfa.*” **Aroma 3v23, 6v23**


Simungapeze moyo wosatha pokhala munthu wabwino, kupita ku tchalitchi, kapena kubatizidwa (**Aefeso 2v8-9**).



Moyo wosatha kumwamba ndi mphatso koma tchimo limatilekanitsa ndi Mulungu. Kuchimwa ndiko kusankha kuchita zinthu zomwe tikudziwa kuti ndizolakwika ... kusilira, udani, umbombo, ndi zina zotero.

Baibulo likufotokoza kuti “*onse anachimwa ndipo anaperewera pa ulemelero wa Mulungu*” komanso “*mphotho ya uchimo ndi imfa.*” **Aroma 3v23, 6v23**


Simungapeze moyo wosatha pokhala munthu wabwino, kupita ku tchalitchi, kapena kubatizidwa (**Aefeso 2v8-9**).



Muchikondi chake Mulungu wapereka njira ya chikhululukiro. Baibulo likuti, “*Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha kuti yense wokhulupilira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha.*” **Yohane 3v16**

Pa mtanda Yesu anatenga chilango chathu ndipo anauka kwa akufa kutengera chikhululukiro cha machimo athu komanso moyo wosatha, ngati tilapa ndikudalira Iye.


### CHIKONDI CHA MULUNGU



Muchikondi chake Mulungu wapereka njira ya chikhululukiro. Baibulo likuti, “*Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha kuti yense wokhulupilira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha.*” **Yohane 3v16**

Pa mtanda Yesu anatenga chilango chathu ndipo anauka kwa akufa kutengera chikhululukiro cha machimo athu komanso moyo wosatha, ngati tilapa ndikudalira Iye.


### CHIKONDI CHA MULUNGU



Chisankho ndichanu. Yesu akuti “*Ine ndine njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine.*” Baibulo likuti, “*Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.*” **Machitidwe 2v38**

Ngati mukana kulandira chikhululukiro chaulere chochokera kwa Mulungu, zikutanthauza kuti mwasankha kukakhala umuyaya wosiyana ndi Mulungu, ku gehena.


### Lero ndi tsiku la chipulumutso chanu



Chisankho ndichanu. Yesu akuti “*Ine ndine njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine.*” Baibulo likuti, “*Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.*” **Machitidwe 2v38**

Ngati mukana kulandira chikhululukiro chaulere chochokera kwa Mulungu, zikutanthauza kuti mwasankha kukakhala umuyaya wosiyana ndi Mulungu, ku gehena.

### Lero ndi tsiku la chipulumutso chanu



### KUWOLOKA MLATHO

Kuti mukhululukidwe, komanso kuti mulandire mphatso ya moyo wosatha, mukuyenera mukhale ndi moyo wodalira Yesu.

Kuti mupulumutsidwe:

- Mukuyenera kulapa (kusiya machimo) ndi
- Kulandira Yesu ngati Mbuye wa moyo wanu.

Mungathe kukhala ndi chitsimikizo chakumwamba tsopano povomereza pemphero ili:

“Okonedwa Mulungu, ndikulapa kuti ndachimwira inu. Tsopano ndikusiya moyo wanga wauchimo ndikubwera kwa inu kuti mundikhululukire.

Yesu, chonde bwerani mu moyo wanga ndikukhala Mbuye wanga. Ndilimbitseni komanso nditsogolereni kusiya moyo wa uchimo ndikubadwa mwatsopano. Zikomo Yesu chifukwa chondikonda ndikubwera mu moyo wanga. Amen.”

### KUWOLOKA MLATHO

Kuti mukhululukidwe, komanso kuti mulandire mphatso ya moyo wosatha, mukuyenera mukhale ndi moyo wodalira Yesu.

Kuti mupulumutsidwe:

- Mukuyenera kulapa (kusiya machimo) ndi
- Kulandira Yesu ngati Mbuye wa moyo wanu.

Mungathe kukhala ndi chitsimikizo chakumwamba tsopano povomereza pemphero ili:

“Okonedwa Mulungu, ndikulapa kuti ndachimwira inu. Tsopano ndikusiya moyo wanga wauchimo ndikubwera kwa inu kuti mundikhululukire.

Yesu, chonde bwerani mu moyo wanga ndikukhala Mbuye wanga. Ndilimbitseni komanso nditsogolereni kusiya moyo wa uchimo ndikubadwa mwatsopano. Zikomo Yesu chifukwa chondikonda ndikubwera mu moyo wanga. Amen.”

Mulungu amadziwa mtima wanu. Ngati mwalapa kwathunthu, tsimikizikani kuti machimo anu akhululukidwa ndipo mwabadwa mwatsopano, tsopano ndinu mwana wa Mulungu. Mwina simungamve kusinthika tsopano, koma lonjezo la Mulungu ndi ili: “*onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu.*” **Yohane 1v12**

Kubadwa mwatsopano kutanthauza kuyamba moyo watsopano ndi mphamvu ya Mulungu kukuthandizani kuyenda ndi Yesu mu Chiyero. Mulungu anatomiza Mzimu Woyera kukhala mwa inu, kukupatsani mphamvu yogonjetsa tchimo. Munjira iyi, mungathe kukana tchimo liri lonse kuphatikiza kuledzera, chiwerewere, miseche, kusilira ndi zina zotero. Musakayikire mphamvu ya Mulungu, Iye ndiokhoza kukuyeretsani ku tchimo liri lonse. Baibulo likuti, “*zonse ndizotheka ndi Mulungu*” komanso “*ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi*

Mulungu amadziwa mtima wanu. Ngati mwalapa kwathunthu, tsimikizikani kuti machimo anu akhululukidwa ndipo mwabadwa mwatsopano, tsopano ndinu mwana wa Mulungu. Mwina simungamve kusinthika tsopano, koma lonjezo la Mulungu ndi ili: “*onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu.*” **Yohane 1v12**

Kubadwa mwatsopano kutanthauza kuyamba moyo watsopano ndi mphamvu ya Mulungu kukuthandizani kuyenda ndi Yesu mu Chiyero. Mulungu anatomiza Mzimu Woyera kukhala mwa inu, kukupatsani mphamvu yogonjetsa tchimo. Munjira iyi, mungathe kukana tchimo liri lonse kuphatikiza kuledzera, chiwerewere, miseche, kusilira ndi zina zotero. Musakayikire mphamvu ya Mulungu, Iye ndiokhoza kukuyeretsani ku tchimo liri lonse. Baibulo likuti, “*zonse ndizotheka ndi Mulungu*” komanso “*ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi*

*olungama Iye kuti atikhulukire machimo athu, ndikutisambitsa, kutichotsera chosalungama chiri chonse.” Marko 10v27 ndi 1 Yohane 1v9*

Ndizofunika kuti muyende monga Yesu anayendera, kukonda Mulungu komanso kukonda m'bale wanu, chifukwa Baibulo likuti ngati mupitiliza kukhala mu uchimo, mutadziwa choonadi, muzakomana ndi moto wa chiweruzo cha Mulungu, ndiwo gehena losatha (**Aheberi 10v26-29**).

Muyenera kuwerenga mawu a Mulungu kuti musanyengedwe. Ngati mulandira chiphunzitso chosiyana ndi mawu a Mulungu (Baibulo), musawalandire. Ikani kudalira kwanu pa Mulungu nthawi zonse, osati pa munthu.

Kuti mukule mu chikhulupiro:

- Werengani mawu a Mulungu.
- Lankhulani ndi Mulungu muzonse.
- Dalirani ndi kumvera Iye.
- Uzani anzanu za Yesu.

*olungama Iye kuti atikhulukire machimo athu, ndikutisambitsa, kutichotsera chosalungama chiri chonse.” Marko 10v27 ndi 1 Yohane 1v9*

Ndizofunika kuti muyende monga Yesu anayendera, kukonda Mulungu komanso kukonda m'bale wanu, chifukwa Baibulo likuti ngati mupitiliza kukhala mu uchimo, mutadziwa choonadi, muzakomana ndi moto wa chiweruzo cha Mulungu, ndiwo gehena losatha (**Aheberi 10v26-29**).

Muyenera kuwerenga mawu a Mulungu kuti musanyengedwe. Ngati mulandira chiphunzitso chosiyana ndi mawu a Mulungu (Baibulo), musawalandire. Ikani kudalira kwanu pa Mulungu nthawi zonse, osati pa munthu.

Kuti mukule mu chikhulupiro:

- Werengani mawu a Mulungu.
- Lankhulani ndi Mulungu muzonse.
- Dalirani ndi kumvera Iye.
- Uzani anzanu za Yesu.

**Video**  
**Are You Truly Born Again?**  
Do you really know what it means to be born again?  
Please watch the following short video -  
<http://www.christianissues.biz/areyoutrulybornagainvideo.html>

**FREE BOOKS**  
The Calvary Road, by Roy Hession, and other free books can be downloaded from:  
<http://www.christianissues.biz/freebooks.html>

Contact: Pastor Sam D Phiri  
samdinala@yahoo.com  
0993564671  
0884157558

**Video**  
**Are You Truly Born Again?**  
Do you really know what it means to be born again?  
Please watch the following short video -  
<http://www.christianissues.biz/areyoutrulybornagainvideo.html>

**FREE BOOKS**  
The Calvary Road, by Roy Hession, and other free books can be downloaded from:  
<http://www.christianissues.biz/freebooks.html>

Contact: Pastor Sam D Phiri  
samdinala@yahoo.com  
0993564671  
0884157558

**Mukukhala ndi moyo chifukwa chiyani?**

**Ndinu opulumutsidwa? Mutafa usiku uno mungakafike kumwamba?**

**Mukukhala ndi moyo chifukwa chiyani?**

**Ndinu opulumutsidwa? Mutafa usiku uno mungakafike kumwamba?**